# LERO LEMBO ILI LAKWANITSIDWA

# THIS DAY THIS SCRIPTURE IS FULFILLED

Ingoyimani choncho, ngati mungathe, pamene tikuweramitsa mitu yathu kuti tipemphere.

Okondedwa Atate akumwamba, tiri othokoza usiku uno chifukwa cha mwayi wina wakubweranso kudzalalikira uthenga wa ulemelero wodabwitsa wa Yesu Khristu uwu. Tikukuthokozani Inu chifukwa Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha anthu amene asonkhana kuno mu nthawi ino pamene kukuzizira ndipo iwo chiyembekezero chawo ndi chachikulu, kuyang'anira, kukhulupira kuti chosachitika wamba chiperekedwa kwa ife kuchokera kwa Mulungu. Timabwera ndi chiyembekezo chimenecho Ambuye ku msonkhano uli wonse. Tikuthokozani chifukwa cha utumiki uja tinali nawo usiku wa dzana ku Kachisi. Zikomo chifukwa cha utumiki wa usiku wa dzulo konkuno ndiponso chifukwa cha utumiki wa Lero ku Kachisi. Tikuyembekezera tsopano chimene Inu mungatipatse usiko uno.

Atate, tikudziwa kuti aliyense amene amatha kugwiritsa ntchito manja ake akhoza kusanthula masamba a Baibulo, koma pali m'modzi yekha amene angalichititse kuti likhale la moyo ndi lomveka ameneyo ndi Inuyo. Atate, tikuyang'anira inu kuti muchite zimenezo usiku uno. Tidalitseni mwa njira ili yonse. Mitima yathu ndi yozala ndi chimwembe pamene tidzakomana Naye maso ndi maso - Iye amene takhala tikumukonda zaka zonsezi. Otembenuka kumene ambiri, Ambuye, akupezeka. Tikumva kuti gulu la anthu fote kapena fifite, libatizidwa m'mawa uno mu Dzina lanu amene adzipereka usiku wathawu. O Mulungu, chonde pitirizani, tikukupemphani, mpaka mbewu yosankhidwiratu ya Mulungu yonse ikaone kuwala kwa Uthenga ndi kudza m'khola lanu.

Tikukufunsani Inu kuti mutibise usiku uno kutseri kwa Mawu; mutichititse khungu kwa zinthu za dziko lapansi ndipo mutilore tizingoona Yesu. Pachitikenso pakati pathu usiku uno zomwe zinachitika pa phiri la kuwalitsidwa

kwanu, kuti tisaone munthu wina aliyense koma Yesu yekha. Tikupempha izi mu Dzina Lake mwa ulemelero wa Iye, ndi chitsimikiziro cha uthenga Wake. Amen. Mukhoza kukhala pansi.

Ndingotembenuza cholankhulirapochi, kapena gomeli, cha kumbaliku pang'ono ngati kuli kololedwa kutero, kuti ndizikhoza kuwona mbali zonse za msonkhanowu. Ndikuganiza kuti ndikhoza kumayenda ndi zolankhulirapozi mosavuta. Chahwino, yembekezani pang'ono.

Tikukupatsani moni kuchokera mu holo yaikulu usiko uno, anzathu ku Arizona, California, Texas ndi mbali zonse za America amene mwatchera matelefoni. Kotero tikudalira kuti Mulungu atidalitsa.

Kodi mungandimve kumbuyo kwa holo cha kumanzereko? Chabwino, tsopano akuyamba kuyesa mawaya a matelefoni ngati zikugwira ntchito bwino.

Aliyense ndi wokondwa usiko uno? Chabwino. Mbali iyi? Amen. Ndiri wokondwa kukuonani mutakhala motakasuka. Ndipo mawa usiku ngati anthu azingochulukirabe, padzakhalanso telefoni yotcheredwa - iliponso usiku ono; ndikuganiza kuti ena akumvetsera pakali pano ku Kachisi. Ndipo mawa msonkhano wa m'mawa sungachitikire ku Kachisi, chifukwa kudzakhala osamalira za maluwa akukongoletsa kachisi pokonzekera chikwati chimene tidzakwatitsa mawa madzulo. Ndipo asamutsira msokhano wa m'mawa ku tchalitchi kwa m'bale Ruddle (m'modzi wa oyanjana nawo athu.) Ndiko kutsata msewu waukulu pa-62. Kodi mwalengeza kale? Alengeza kale. Ndipo malo akakachepa kumeneko, tidzatapa ena ndi kuwatumiza kwa mtumiki wina m'bale Junior Jackson ku Clarksville. Chifukwa chimene tasankhira kwa m'bale Ruddle ndi chifukwa kuti ali pafupi ndi kuno ndipo - tinawona kuti sizidzativuta kutero. Ndipo tisamalira zonse mwa njira yake. Onetsetsani kuti onse adzabatizidwe mawa, ndipo ndikuyembekezera kuti pakhala ena handirede imodzi kapena mahandirede awiri amene ati awonjezereke pa iwo odzabatizidwa mawa.

Ndipo tsopano mawa usiku...sindimakonda kulengeza chiri chonse chodzachitika mtsogolo, koma ulaliki wa usiku wina kapena tsiku lina, ndikufuna kudzalankhula pa mutu

wa "Kodi Melchisedeki uyu anali ndani?" Chifukwa ndi phunziro limene - ndikuganiza kuti ife tikukhala munthawi imene mavumbulutso awa amene akhala akutipatsa mafunso m'mibadwo yonse kuti, "Kodi munthu ameneyu anali ndani?" Ndipo ndikukhulupira kuti Mulungu ali ndi yankho kuti ndi yani iyeyu. Ena...koma papezeka...pamene pali funso, payenera kukhala yankho lake limene liri lolondola. Sipangakhale funso pasanakhale yankho poyamba.

Tsopano, tikudalira kuti Mulungu atipatsa madalitso usiku uno kuchokera pa Mawu Ake amene titi tiwerenge.

Ndipo munali ndi...Billy wandiuza kuti munali ndi chiyanjano chabwino ndi anthu amene amayang'anira malo oyimikapo magalimoto, a polisi ndi aliyense. Pitirizani kutero; zimenezo ndiye zabwino kwambiri.

Tikuyembekeza kudzaona nthawi (mwina mtsogolo posachedwapa) pamene mwina tidzabweretsa chihema ku mzinda chimene tidzachiyimika pa bwalo la mpira kumene tidzakhoza kukhalako mwa nthawi yotalikirapo, mwina chitsitsimutso chongopitiriza cha masabata atatu kapena anayi. Ndipo pano, tangofuna kungodziwanapo wina ndi nzake, kenako tisazikana ndi kubwerera kwathu. Koma ndikukhumba ndidzakhale mowirikiza, nthawi ina pamene, sindidzalekezanso usiku kapena masiku awiri, Koma kungokhala, ndi kuphunzitsa usiku ndi usana mosalekeza. Mwina wena napita kuyumba kukadyetsa nkhuku, kukakama mkaka, nabwerera sabata linalo msonkhano ukupitirirabe. Ndimakonda zoterozo. Kotero Ambuye akhale nanu.

Tsopano, ndisanapite, kapena m'mawa wa la Mulungu kapena usiku wake, kapena nthawi ina yake (pa maulaliki amenewa), ndikudziwa inu mukuyembekezera kumva uthenga wa "Choonadi cha Ukwati ndi Kulekana", limene liri limodzi la mavuto aakulu a masiku ano. Ndiye ine... Ponena zoona monga pameme ndayima panomu, ndikukhulupirira kuti yankho lolondola liri mu Mawu a Mulungu, ndipo ndikukhulupira kuti...ndi chimene ndinalonjezera kuti ndibweranso.

Tsopano ngati, podziwa...Momwe ine ndikudziwira, ndidzakhale ndi msonkhano wina-pa kutuluka kwa dzuwa ndi pa Easter Sunday; kotero tidzalengeza mtsogolo ndi kuyesa

mwina kupeza holo ngati kudzatheka, kapena kwina la Mulungu - mwina loweruka ndi la Mulungu. Pamenepo tingopita ndi kubwerera chifukwa nthawiyi yayandikana... ndifunsa poyamba dongosolo la misonkhano yanga ya ku California. Ndipo zitangotha izo, ndidzayenera kupita ku Africa. Kotero khalani a tcheru ndipo muzindipempherera.

Tsopano, usiku uno ndikufuna kuti mumvetse gawo la Mawu a Mulungu amene akupezeka pa chaputala 4 cha Luka - chaputala 4 ndipo tiyambira pa vesi 16. Yesu akulankhula: "Lero lembo ili lakwanitsidwa m'makutu anu."

Tsopano, tikufuna kutengapo mutu wa momwe Mawu a Mulungu ali opambana. Tsopano, tonse tikhoza kudziwa chimangirizo chokha, koma zimatengera mphamvu yoyenera kugwiritsa ntchitoyo. Tikhoza kudziwa chimangirizo cha ntchini (galimoto), koma zimatengera mphamvu yina kuti ikachititse magudumu kuti ayende.

Tsopano Yesu anabwerera - ku Nazareti kumene Iye analeredwerako. Kupitirira ndi Malembo m'musimo tipeza kuti anati, "Ife tamva kuti munachita zakuti zakuti ku Kaperenao; tsopano chitani tiwone kumudzi kwano kuno."

Yesu anati, "Mneneri amakhala wopanda kulemekezedwa kumudzi kwao kokha. Ndipo zoonadi uko ndi kumene iye analeredwa komwe kunali anthu omudziwa. Ndipo kumeneko Iye analibe dzina labwino ndi pachiyambi pomwe pakuti Iye anabadwa opanda bambo a pa dziko lapansi. Anali kumutcha Iye mwana wa pathengo - kuti Maria anapezeka ali ndi pakati asanakwatiwe, modziwika kwa onse, ndi Yosefe. Koma izi sizinali motero; ife tikudziwa kuti sichoncho.

Ndipo pa Lembo ili, chimene chinandichititsa kuti maso anga ayang'ane pa ilo, ndi china chimene chinachitika posachedwapa ku Phoenix, Arizona. Linali tsiku lotsiriza la msonkhano umene ndimalankhulapo ku International Convention of the Full Gospel Business Men, ndipo pa msonkhano umenewu panali mulendo wathu amene anali Bishop wa Katolika, amene ali m'modzi wa Chaldean Rite ya Apostolic Catholic Church - Olemekezeka kwambiri John S. Stanley, O.S.D. Iye ndi archbishop wa Metropolitan United States mu Mpingo wa Katolika. Zimenezi zina-

lembedwa pa khadi lake - ndi address yake.

Ndipo iye anali mulendo wa Christian Business Man, ndipo ndinali nditamuona iye kumeneko dzulo lake. Ndipo pamene ndinali kulankhula Loweruka ndikukhulupira unali usiku kapena m'mawa pa chakudya cha m'mawa, ndipo - pamene ndimalankhula iye - amangondiyang'anitsitsa ine. Ine ndinaganiza, "Munthu uyu akusutsana nane pa zonse zimene ndikulalikira." Ndipo - mukudziwa, mukadakhoza - mukanangomuwona iye; amangoyang'ana m'mwamba ndi pansi, koma sindikudziwa bwino bwino chimene amalingalira.

Kotero Lamulungu madzulo pamene ndinayamba kulankhula, ndinkatenga mutu wa nkhani ya Birth Pains (Mavuto a Pobereka) - pamene Yesu anati monga mzimayi amene akuvutika pobereka mwana, amavutika pobereka mwana, amavutika ndi kupwereka. Koterono ndinkati ndilankhule pa mutu wa Birth Pains (phunzitso). Kumati kuti dziko liri pa kuvutika kwa kubereka tsopano. Lakale liyenera kuchoka kuti la - tsopano libadweno; monga momwe mbewu imayenera kuvunda kotero kuti papezeke moyo watsopano. Ndipo momwe kupweteka uku, kuwawa kwa pobereka, kunakhuza dziko pa Nkhondo ya Dziko lonse Yoyamba (World War I). Dziko monga mkazi linali pa nthawi ya kupweteka kwakukulu, chifukwa anali ndi gasi wa poisoni ndi zina zotero zimene zikanakhoza kuwonongeratu dziko. Ndipo pa Nkhondo ya Dziko Lonse Yachiwiri (World War II) kuwawa kwachiwiri kunaligwiranso; anali ndi zida zokhoza kugumula ndi bomba la atomic. Silingapirirenso kuwawa kwina kwa kubala uku. Ndi zida za ma misayelo (missiles) ndi zinthu zamakono, nkhondo ina imodzi yokha ikhoza kuliphulitsa, pakuti tsopano lidzakhala likubala ndipo kudzakhala dziko lapansi latsopano. Baibulo linati padzakhala dziko latsopano.

Pansi pa Uthenga wa m'neneri aliyense wa Aisrayeli panali kuwawa kwa kubereka, chifukwa anereri awa amapeza anthu ophunzira za zipembezo ndi azibusa atasandutsa mpingo kukhala bungwe. Ndipo pamene mneneri amadza ndi ATERO AMBUYE, anali kugwedeza mipingo nikhala ndi kuwawa kwa kubala. Potsiriza kuwawa kwa kubala kunapitirira mpaka kunabereka Mwana wa Uthenga Wabwino amene anali Mawu omwe atasandulika thupi.

Kotero mpingo zedi uli pa kuvutika kwa pobala usiku unonso kuti ubereke Mwana - Mwana wa Mulungu adzenso. Ophunzira za zipembezo zathu, machitidwe onse, madinomineshoni athu onse avunda kwa thunthu. Kotero tiri pa kuwawa kwa pobala, ndipo Uthenga wochokera kwa Mulungu nthawi zonse umapatsa mpingo kupweteka kwakukulu. Koma patapita kanthawi ubereka mkwatibwi amene adzabweretse Yesu Khristu kwa Mkwatibwi Wake.

Ndipono, poganiza kuti munthu uyu anali kutsutsana nane kwambiri, pamene ndinaimirira kuti ndilalike Uthenga umenewu, ndinatsegula mu Baibulo langa kuti ndipeze pa malo amenewa, ndinayamba kuwerenga pa chaputala 16 ndipo vesi limene ndimalifuna silinapezeke! Kotero ndinaganiza 'za chilendo'. Ndinafunanso; komabe panalibe. Ndipo m'bale Jack Moore ochokera ku Shreveport, Louisiana mbale wanga wa pamtima, anali pamenepo. Ndinati, "Mbale Jack, kodi zimenezo sizimapezeka pa Yohane 16?"

Iye anati, "Inde!"

Ndipo wamsembe wa Katolika uyu ananyamuka pa mpando wake, pakati pa azibusa pafupifupi wani handiredi anali paguwapo, anayenda mpaka pafupi nane, ndi zovala zake zonse, mikanjo ndi mitanda ndi zina zotero, nafika mpaka pafupi kwambiri ndi ine; nati, "Mwana wanga, dekha. Mulungu ali pafupi kuchita kanthu."

Ndipo ndinaganiza, "Bishopo wa Katolika kundiwuza ine zimenezo!"

Iye anati, "Werenga zimenezo kuchokera mu Bukhu langa."

Ndipo ndinawerenga Malembo kuchokera mu Bukhu lake, ndipo ndinatenga mutu wa nkhani yanga ndipitirira; kulalikira ulaliki wanga.

Kenako, nditatsiriza, iye anadzuka, pamenepo ine nditachokapo nati, "Pali chinthu chimodzi chimene chiyenera kuchitika. Chitatha chimenecho, mpingo uyenera kulowa mu chitsokonezeko chachikuluchi, ife tiyenera kuchoka muchitsokonezeko chimene chiri mu mpingo." Kotero chimodzichi kapena chinzakecho.

Ndipo ine - ndinali paulendo wanga wakumudzi (Kubwerera ku Tuscon) usiku umenewo, ndipo ana ankalirira sangweji, ndipo ndinayima kuti ndigule sangweji pa malo ena aang'ono ogulitsirapo. Ndipo mkazi wanga anati, "Billy, sindinayambe ndakuwona ndi manjenje m'moyo wanga wonse ngati lero momwe umafunafuna mu Baibulo lija." Nati "Kodi sizinakuchititise manjenje iweyo?"

Ndinati, "Ayinso." Ndinati, "Ndimadziwa kuti zinalembedwa pena pache; kunangokhala kuti pepala limenelo panalibe. Anagodinda molakwitsa."

Komabe, ndinakhala pansi ndi kusanthulanso. Mwangwiro bwino bwino, koma chaputala 16, mwa gawo - gawo lake lina linali ma inchesi atatu kuchokera pansi, pamwamba pa chaputala 17, mbali inayo inali chimodzi modzi; ndipo pokhala Baibulo latsopano, mapepala awiri anagophatikizana kwambiri, ndipo ndinali kuwerenga pa chaputala 17 m'malo mwa 16.

"Chabwino," Ndinati, "Zonse ziri bwino. Pali chifukwa chache."

Ndipo momwe inu mungamvere Liwu mosavuta, LIWU linadza kwa ine niliti, "Iye analowa Ku Nazarete kumene Iye analeredwerako nakalowa mu sunagoge monga momwe unali mwambo. Ndipo ansembe anamupatsa Iye Malembo kuti awerenge, ndipo Iye anawerenga malembo, anakhala pansi, nabwezera Baibulo, Bukhulo kwa ansembe, nakhala pansi. Ndipo maso a anthu osonkhana anali pa Iye ndipo mawu opambana anatuluka pakamwa pake nati, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa."

Lero Lembo ili lakwanitsidwa" Malembo amangokhala olondola kukwaniritsika Kwake! Ngati mutavundukula pa Yesaya 61:1-2 ndi pamene Ambuye wathu anali kuwerenga - Yesaya 61:1-2. Koma pakati pa vesi la Yesaya 61, Iye analekeza pamenepo nati, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine ndilalikire chaka chovomerezeka." Ndipo analekeza chifukwanji? Mbali inayo, 'kubweretsa chiweruzo', siinali yokhuzana ndi kudza koyamba kwa Iye, koma kudza kwake kwachiwiri! Mukuona, silimakhuza nthawi imeneyo; umu ndi momwe Malembo samaphonyetsera. Nthawi zonse ali angwiro Yesu analekeza pamene Malembo analekezera,

chifukwa chimenecho ndi chimene chinayenera kukwaniritsidwa pa moyo Wake.

Tsopano, pa za kudza koyambako... Kudza kwachiwiri adzabwera ndi chiweruzo kwa dziko lonse lapansi, koma osati ntawi imene ija. Iye anayenera kulalikira "chaka chovomerezeka."

Taonani, Mesiya, kuyima pa guẃa nadziwulula Iye mwini ndi Mawu a Lonjezo a mbadwo umenewo. Zachilendo - Mesiya kuyima pamaso pa mpingo! Ndipo taonani Mawu opambanawa, pamene Iye anati apa, "Kudzalalikira chaka chovomerezeka."

Chaka chovomerezeka, momwe tidziwira ife tonse owerenga Baibulo, chinali chaka cha ufulu (Jubilee); kuti pamene akapolo onse ndi akayidi, momwe iwo anali... atatengedwa ukayidi, ndipo anali kuyenera kupereka mwana wa mwamuna polipira ngongole; kapena mwana wamkazi polipira ngongole, ndipo iwo anali mu nsinga. Ngakhale atakhala mu nsinga nthawi yotani, Kaya anayenera kukhala kumeneko Nthawi yotani, pamene chaka chaufulu chifika, pamene lipenga limamveka, munthu aliyense amakhoza kupita mwa ufulu ngati amafuna kukhala mfulu. Anali mfulu; samakhalanso kapolo.

Koma ngati mutafuna kukhalabe kapolo, kotero mumayenera kutengedwa kunka nanu ku Kachisi, mumayima pa nsanamira ya Kachisi, ndipo amatenga chisongole naboola khutu lanu. Kotero mumayenera kumutumikira mbuye wanu masiku onse a moyo wanu.

Chisanzo changwiro ndi uthenga wa Yesu Khristu. Pamene kulalikidwa, chaka chovomerezeka ndi nthawi ya ufulu kwa aliyense, ngakhale muli yani, kaya khungu lanu ndi lotani, ndinu wa mpingo wanji. kaya munalowelera mu machimo chotani, kapena chovuta chanu ndi chiyani, mukhoza kukhala mfulu pamene mumva - Lipenga la Uthenga wa Mulungu litalira! Ndiwe mfulu! Koma ngati mulozetsa nsana wanu kwa uthenga ndi kukana kuumvera, taonani, mumabowoledwa khutu ndi chisongole. Zimenezo zimatanthauza kuti, inu mwawoloka nzere wa pakati pa chisomo ndi chiweruzo ndipo simudzamvanso Uthenga! Simudzasinthanso; Iwe uzikhala kapolo wa zimene ukuchitazo ma-

siku onse amoyo wako, ngati wakana kumvera chaka chovomerezeka.

Tsopano, gawo lina la ichi, monga ndinati, silinayenera kuwerengedwa, chifukwa Mesiya amene akudzayu, nthawi ino ndi pamene adzabweretsa Chiweruzo.

Tsopano, anthu aja analephera bwanji kuwona chimene Iye anali? Anaphonya bwanji ichi? Zikanatheka bwanji pamene zonse zinali zomveka bwino ndi zooneka? Anaphonya bwanji kuwona pamene Iye... Tangoganizani Mawu ake! Tangolingalirani! "Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu!"

Ndani ananena zimenezi? - Mulungu Mwini wake, Amene ali womasulira wa Mawu Ake omwe. "Lero Lembo ili lakwanitsidwa." Koma iwo analepherabe kuwona ichi.

Ndi ngozi yotani imeneyo kuti ichitike, koma zinachitika. Zachitikapo kambiri mbiri. Zingachitike bwanji? Ndithudi, monga momwe zinachitikira pa nthawi zina zambiri, pokhulupira tanthauzo la munthu pa Mawu. Izo ndi zimene zinachititsa. Okhulupira amene mu masiku amene aja (anthu otchedwa okhulupira) anali kutenga kumasulira kumene ansembe anawauza pa malembo. Kotero Yesu, posakhala wa gulu lina liri lonse kapena mabungwe awo, Iye anakanidwa chiyanjano ndi gulu lawo. Ndipo kotero, sakanatha kudziyanjanitsa ndi Iye, chifukwa Iye anali wosiyana ndi iwo. Umunthu wa Yesu Khristu unali wosiyana ndi ena kotero kuti aliyense sanayenera kuphonya kumuwona kuti anali Mwana wa Mulungu, chifukwa Iye anali wofanana mwa ngwiro ndi zimene Malembo analembedwera za Iye! Njira imene Mkhristu aliyense amaziwikira - pamene moyo wake ufanana ndi zimene Akhristu ayenera kuchita.

Momwe Iye amakhoza kuyima pamenepo nati, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa! pa maso panu!" Zopambana bwanji! Zomveka kwambiri, ndipo koma anthu amene aja sanamumvetsa. Bwanji? - ndi chifukwa iwo anatenga matanthauzo a dongosolo la ansembe amene anali kuwamvera. Ndipo Mbiri nthawi zonse imadzibwereza, ndipo Malembo ali atanthauzo la pawiri ndi vumbulutso pawiri kwa iwo!

Pakuti kuli ngati momwe Baibulo limati, "Ndidzayitana Mwana Wanga kuchokera ku Egypt" (Kukamba za Yesu). Onani milozo yothandizira mu mbali ya Baibulo lanu ndipo mupezanso kuti akukamba za Yakobo - Malembo omwewo. Yesu anali Mwana Wake wa mwamuna wamkulu. Yakobo anali Mwana Wake amene anamuyitana kuchokera ku Egypt, amene milozo ya Scofield Baibulo ndi milozo ina yonse imatero, chifukwa Malembo amenewo ankanena za zimenezonso, kotero anali ndi mayankho awiri. Linali ndi yankho kwa Yakobo wotulutsidwayo ndi kwa Yesu wotulutsidwanso.

Koteronso lero! Ndi chifukwa kuti tiri pa chisokonezeko, kuti anthu akulephera kuwona Choonadi cha Mulungu, chifukwa kwachuluka matanthauzo opekedwa ndi anthu pa Mawu a Mulungu." Mulungu samafuna aliyense kuti amasulire Mawu Ake! Iye amadzimasulira yekha!
Mulungu anati pachiyambi, "Kuwale" ndipo kunawala. Zimenezo sizisowa wina wotanthauzira.

Pamene - Tanthauzo la Mulungu la Mawu Ake ndi pamene Iye aliwonetsera ndi kutsimikizira ilo kuti liri choncho! Limenelo ndilo tanthauzo Lake - pakukwaniritsa! Limenelo ndilo tanthauzo la Mulungu, ndi pamene Iye achititsa Mawu Ake kukwaniritsidwa; pamenepo Iye akumasulira kwa inu.

Monga ngati kukanakhala kulibe kuwala ndipo Iye nati, "Kuwale" ndipo nkutero; zimenezo sizingasowe kumasulira kwa aliyense. Koma ife timalandira nzeru za anthu ndi kusakaniza. Ndipo pamene mutero - mumachoka pa nzere. Zakhala choncho nthawi zonse.

Koma ndikuganiza kuti, miyoyo yawo inakhuzidwa motani? Tangoganizirani! Mesiya! Iwowa analephera bwanji kumuwona Iye? - chifukwa atsogoleri awo amene anayenera kumudziwa Iye, amene anayenera kukhala atamwera Malembo, iwo anamuchepetsa Munthu uyu nati, "Iyeyu ndi Mwana wapathego - kuyamba ndi kuyamba." Ife sitingakhulupire zimenezo. Zaka zapitapo ife sitikukhulupira zimenezo; tikhoza kuphedwa pakungonena kuti Iye anali Mwana wobadwa mwa namwali! Ndipo kudzachitika tsiku lina kuti zinthu zomwe tikumuwona Yehova akuchita lero, anthu a mu mibadwo ikudzayo, ngati ilipo, adzafera zin-

thu zimene tikukamba lerozi! Mudzatero pamene chilembo cha chirombo chidzagundika, ndipo inu simudzaloledwa kulalikira Uthengawu chotere.

Pamene chigwirizano cha mipingo pamodzi chidzayamba, chimene chayamba kale pakali pano kwa mipingo yonse ya pa dziko lapansi, inu mudzatsindikiza umboni wanu ndi moyo wanu womwe pamenepo. Muyenera kukhulupira pakali pano. Ngati ansembe amene ankamunyoza Iye aja akanawuka lero sakanamunyozanso ayi.

Koma inu mukuti, "Ndikanakhalako ine pa nthawi imeneyo, mwenzi nditachita chonchi chonchi."

Inu, umenewo sunali mbadwo wanu, Koma uno ndiwo mbadwo wanu! Ino ndiyo nthawi yanu!

Mukuti, "Komatu Iye akanakhalapo..."

Baibulo likuti, Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse - ali yemweyo; Kotero Iye ali pano. Koma Iye ali pano... Monga pamene dziko latukukira ndi kukhala lotchuka ndi lophunzira kwambiri, Iye ali pano mwa ma onekedwe a Mzimu, umene sangawuphe kapena kuwuyika kumanda. Iye anafa kamodzi, Iye sangafenso kachiwiri. Iye anayenera kusandulika thupi ndi cholinga chakuti Mulungu akaphe tchimo mu thupi. Koma nthawi yino Iye sangafenso; Iye ali Mzimu Woyera tsopano.

Tsopano, tingaganizire momwe iwo aja analiri nazo zomusutsa Iye. China mwaizo, ndi kuti Iye sankajowina magulu awo. Kotero mukuwona, chimenecho chinamupangitsa Iye kukhala munthu woyipa. Iye samajowina - mabungwe awo, samajowina unsembe wawo, ndipo analibe nazo ntchito zimenezo. Ndipono pambali pa zonsezo, Iye anali kuyesa kuphwasula zimene iwo anazimanga!

Iye anapita ku Kachisi. Timamutcha Iye Munthu wofasa; analidi koma nthawi zambiri sitimamvetsa chimene kufasa kumatanthauza. Iye anali Munthu wa chifundo, Komabe ife nthawi zina sitimamvetsa kutanthauza kwa chifundo osati kuti chisoni cha umunthu ndicho chifundo, koma chifundo ndicho kuchita chifuniro cha Mulungu. Iye anapyola thamanda la Betsaida, polowera ku thamanda; panagona

anthu, chinantindi si anthu angapo ayi, koma panagona chinantindi - olumala, akhungu agonthi, opunduka. Ndipo anali wa chifundo kwa anthu nthawi zonse ndipo Iye anapita kwa munthu m'modzi amene sanali wopunduka, wakhungu, wosamva, kapena wolumala ayi mwina iyeyu anali ndi vuto la kungosokonezeka; mwina anali ndi kachiwanda kongomupusisa pang'ono; anali wotero mwa zaka 38 sichimamusautsa iye kwambiri, sichikanamupha konse. Iye ankangokhala pamphasa yake.

Ndipo iye anati, "Kodi ukufuna ndikuchiritse?"

Ndipo munthuyu anati, "Ndiribe munthu wakuti angandinyamulire m'madzi, ndipo pamene ndifuna kulowamo, wina amadza nandipitirira ine."

Mukuona, iye ankakhoza kuyenda; ankakhoza kuwona; ankakhoza kuchita chimene angafune, koma anangokhala wofooka.

Ndipo Yesu anati kwa Iye, "Nyamuka! Tenga mphasa yako nupite kwanu!" Ndipo Yesu anafunsidwa pa zimenezi. Pakuti inu mukukumbukira Malembo anatero...

Zosadabwitsa. Ngati Iye akanadza ku Jeffersonville usiku uno ndikuchita zotero akanamunenabe. Koma kumbukirani, Iye anadza kudzachita chinthu chimodzi - chinali chifuniro cha Mulungu. Tsopano izo zimapezeka pa Yohane 5:19; mupeza yankho lanu. Iye anati, "Indetu, indetu ndinena kwa inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iye yekha koma chimene awona Atate akuchita, ndi chimene Mwana achita."

Tsopano, iwo anayenera kudziwa kuti chimene chija chinali chitsimikizo cha uneneri wa Mose. "Pakuti Ambuye Mulungu wanu adzakuwukitsirani mneneri monga ine."

Mukhoza kuwona pamene Iye anawona munthuyu Iye anati... Yesu anadziwa kuti iyeyu anali mu khalidwe limeneli zaka zambiri. Iye pokhala Mneneri, Iye anawona munthu uyu mu chikhalidwe ichi napita kwa iye - napyola pakati pa anthu onsewo, kujowa pakati pawo mpakana pamene anapeza munthu ameneyu. Kupyola anthu opunduka, osamva, akhungu ndi olumala, komatu ameneyu ndi munthu

wozaza chifundo, koma chifundo ndicho kuchita chifuniro cha Mulungu.

Tsopano, tikumupeza, pamene Iye sakanajowinana nawo, Iye analibe nazo ntchito zimagulu zawo, ndiye Iye anali wakunja kwa iwo. Iye sanakakhoza konse... Komanso Iye anapita ku kachisi tsiku lina. Mwamunayu anapita uku napeza nyumba Ya Mulungu itangokhathamira ndi zoyipa monga masiku ano. Iwo anali kugula ndi kugulitsa, kusintha ndalama, ndipo Iye anagubidiza magome andalama, natenga zingwe nazipota nakwapula osintha ndalama kuwatulutsa mu kachisi nayangana pa iwo mwa ukali! Ndipo anati, "Kunalembedwa (Aleluya). Nyumba ya Atate wanga ndi nyumba yopemphereramo ndipo inu mwayisandutsa phanga la akuba! Ndipo inu, ndi miyambo yanu, yapangitsa malamulo a Mulungu kukhala opanda mphamvu."

O, gulu loterelo kodi likanatha kumukhulupira Iye? Ayi, wawa! Anali muzithaphwi za mabungwe ndi zonyansa za nthawi yawo mwakuti anangozizidwa ndi chipembezo mpakana kuti sukanakhoza kupeza kugunda kwa mphamvu ya Mulungu Wamphamvu zonse mwa iwo. Zosadabwitsa kuti kamzimayi kanakhoza kukhuza chovala Chake nikapeza machiritso pakutero, pamene msirikali wolezera amakhoza kulavulira pa nkhope yake koma osakhuzidwa ndi mphamvuyo! Zimatengera chomwe iweyo ukudzera; Zimatengera chimene iweyo ukufuna kuwona. Pamene upita ku tchalitchi zimatengera chimene ukunkera.

Tsopano, tikumuwona Iye atayima paja. Mosakayikitsa kuti anthu anali atamuchenjeza Iye kale - kuchenjezedwa - ansembe anali atachenjeza anthu kuti, "Tsopano, Iyetu abwera kuno tsiku la Sabbata likudzali, ndipo akatero, osadzamumvera Iye. Tsono, mukhoza kudzabwera ndi kukhala pansonkhanowo, koma osamvera zolankhula zake, chifukwa Iye si wa gulu lathu. Iye ndi wakunja kwa ife. Alibe khadi la mapangano; ndiponso alibe... zipepala za bungwe lakelo. Alibe china chiri chonsecho."

"Ndi ndani iyeyo?"

"Kamwana kena kache kamene kanabadwa mwapathengo ku banja la kalipentala - mwakuti mayi wake anali ndi pakati iwo asanalowe banja, ndipo akuyesa kubisa nama-

nyengezera kuti anapatsidwa pakati mwa uzimu. Ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adza Iye adzatsika kuchokera mu khonde la Kumvamba nafika kwa wansembe wamkulu nati, "Ndabweratu, Kayafa."

Koma tikupeza kuti Iye sanabwere mwa njira imeneyo, chifukwa sikunalenbedwe mu Mawu motero! Zinali miyambo yopangidwa imene inawachititsa iwo kukhulupira zimenezo. Mawu amati kuti Iye anayenera kudza mwa njira yomwe anadzerayo! Ndi uyo tsopano amene anayima kuwerenga Mawu anati kwa iwo, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu," Komabe analephera Kumuwona Iye kapena kumudziwa Iye, monga momwe anachitira mu mibadwo ina yonse.

Nowa akanakhoza kulankhula chimodzi modzi pa tsiku limene analowa mu chombo khomo litatsekeka. Nowa akanakhoza kutsegula zenera la pamwamba pa chombo, kuyang'ana kunja pa anthu osonkhanawo (Kumbukirani, Mulungu anatseka chitseko) ndipo akanakhoza kunena kuti, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu!" Koma nthawi anali itatha kwa iwono. Iye anali atalalikira zaka 120 kuyesetsa kuwayitanira anthu kuti adzalowe mu chombo chimene iye anachimanga nawawuza iwo Malembo kuti ATERO AMBUYE kugwa mvula! Koma, iwo anadikira nthawi yayitali. Komano Nowa akanakhoza kunena mosavuta kuti, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa."

Mose, tsiku lija pamene Lawi La Moto linatsika pa Phiri la Sinai ndi kuchitira umboni ku zimene amalankhula, Mose akanakhoza kunena kuti, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa."

Mose, mukudziwa kuti anali mwamuna woyitanidwa ndi Mulungu, m'neneri. Ndipo pamene iye anali kuyitanidwa, pokhala m'neneri, anayenera kukumana ndi zinthu zosachitika wamba kuti akhaledi mneneri. Anayenera kukumana ndi Mulungu pamaso ndi pamaso ndi kulankhula Naye. Ndipo chinthu china, Chimene analankhula chinayenera kuchitika, ngati sichoncho palibe amene akanamukhulupira iye. Kotero, palibe munthu amene ali ndi ufulu wodzitcha yekha choncho, pokhapokhapo iye atalankhulana pamaso ndi pamaso ndi Mulungu kwa yekha ku chipululu chake chake, kumene Mulungu Mwini wake akhoza kukumana naye! Ndi-

po onse azipembezo zachikunja pa dziko lapansi sangathe kumutsutsa iye ndi nthano zawo; pakuti ndi iye amene anali kumeneko, ndipo iye akudziwa kuti zinachitikadi. Mkhristu aliyense ayenera kuchitiridwa zoterezi asanayambe kunena zakuti iye ndi Mkhristu - zokuchitikira iweyo wekha!

Ndimalankhula ndi mzukulu wanga kanthawi kapitako, kamnyamata ka Katolika, amene anati, "Amalume a Bill, ndakhala ndikudumpha kuchokera pa chipilala kupita pa mtengo kunka kuli konse poyesa kuti ndipeze china chake!" Usiku ndi usiku, msonkhano uwu usanayambe, iye wakhala akulira, ndipo mkati mwa usiku wakhala akumalota maloto obwera muno, kuthamangira ku guwa (pamene titalalikira) nayamba kulapa kuti iye anali kulakwa.

Ine ndinati, "Melvin, zilibe kanthu kumene ungayese kupita, mipingo ingati yomwe ungajowine, kangati kamene unganene 'Tikuoneni a Maria', kapena kangati kamene munthu wina angakudalitseni, muyenera kubadwanso mwa Mzimu wa Mulungu! Ndi Chokhacho chimene chimakhutitsa mtima wa munthu." Ine - ndikudziwa ali ndi zina zolowa m'malo mwa kubadwanso masiku ano - umayenera kugwirana chanza ndi alaliki nalemba dzina lako mu bukhu. Koma anzanga, amenewo ndi maganizo a wanthu! Si Choonadi cha Baibulo! Chikanakhala choncho Machitidwe a Atumwi pa chaputala 2 mwenzi akuwerengeka chonchi: "Pamene tsiku la Pentekoste linakwana, abusa anayenda pa mzere nagwirana chanza ndi anthu."

Koma linati, "Pamene tsiku la Pentekoste linakwana (pa kutsegulira kwa mpingo), kunadza mkokomo Kumwamba monga kuwomba kwa mphepo yamphamvu, nizaza nyumba yonse kumene iwo anakhala!"

Umo ndi momwe Mzimu Woyera unadzera pa nthawi yoyamba; ndi momwe umadzera nthawi zonse kuyambira pa nthawi imene ija! Iye ndi Mulungu ndipo sasintha.

Tsopano, zimapunthwisa anthu ena. Iwo amati, zimenezo zinali za masiku wena." Komabe, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawi zonse. Nthawi iliyonse pamene mpingo ulandira Mzimu Woyera, umadza nthawi zonse monga momwe anachitira poyamba, pogwiritsa ntchito ndondome-

ko yofanana - Machitidwe 2:38. Sizinasinthe sizidzasinthanso.

Monga dongosolo la a dokotala pa matenda, iye amalemba mankhwala ofunika kwa matendawo (dokotalayo amachita izi), ndipo ukatengera chipepalacho kwa munthu wosadziwa bwino za mankhwala, wogulitsa mankhwala pamsewu, ndipo iye amangochulukitsa madzi posungunula mankhwalawo, kotero kuti amangokhala opanda mphamvu mwakuti sangagwire ntchito. Mwina amachulukitsa mankhwala mwakuti zimasanduka poizoni, akhoza kukuphani. Ziyenera kukhala monga momwe a dokotala analembera. Ndipo zolemba za a dokotala za momwe inu mungalandirire Mzimu Woyera zinaperekedwa kwa ife ndi a Dr. Simoni Petro pa tsiku la Pentekoste!

Ndikupatsani dongosolo la mankhwalalo. "Lapani ali yense wa inu ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhulukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera, pakuti dongosolo ili liri kwa iwo amene ali kutali ndi onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana." Dongosolo la Muyaya.

Mose zinamuchitikira yekhanso. Iye anapita mu dziko nayamba kuwuza anthu "Ine ndinakomana ndi Lawi la Moto. Linali kuyaka pa kathengo, ndipo Iye anandiwuza kuti ndikuwuzeni inu kuti, "INE NDINE AMENE NDIRI wati 'Pita; Ine ndikhala ndi iwe. Tenga ndodo m'dzanja lako nuyinyamulire pa Aigupto; chiri chonse chimene unfunsa; chidzachitika."

Mwinabe wamsembe wina anati, "za nkutu!"

Koma pamene anawona zowona zenizeni za ichi - zikuchitika, sakadalimbalimbabe. Anadziwa kuti iye anatumidwa ndi Mulungu.

Ndiye ngati Mose anati anachiwona nachitira umboni za icho kuti ndi Choonadi, kotero Mulungu ali wokakamizika, ngati ichi chiri Choonadi, kuchitsimikizira ndi kukwaniritsira Mawu a munthuyo, Choonadi! Ndi chonchotu.

Ngati Yesu Khristu anayima pamene paja nawerenga tsiku limene lija kuti "Lero Lembo ili lakwaniritsidwa pamaso

panu." Mulungu ali wokakamizika kukwaniritsa Mawu Ake!

Ife tikuyima pano usiku uno kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse! Mulungu ali wokakamizika kutsimikizira motero, chifukwa Iwo ndi Mawu Ake! Tsopano, zimachita chiyani? - Zimatengera chikhulupiro ndi kukhulupirira mwa Iye. Zimatengera chikhulupiro ndi kukhulupirira Mawu Ake kuti ali Choonadi.

Taonani zimene zinachitika pamene Mose anaturutsa ana aja ndi onse amene anamutsata iye. Iwo amene sanamutsate anatsalira mu Egypt, Koma iwo amene anamutsata Mose, pamene anafika pa Nyanja Yofiira ndi kulowa mchipululu, Mulungu anadza pa Phiri la Sinai. Lawi la Moto linayatsa phiri lonse ndipo Liwu linalankhula kuchokera m'menemo, Mulungu napereka Malamulo Khumi! Mose akadakhoza kupita pamaso pa anthuwo nati, "Lero Lembo limene ndinakuwuzani monga mneneri Wake lakwaniritsidwa! Lero, ine ndikuwuzani kuti Mulungu anakumana nanedi pa Kathengo koyaka ndi Lawi Lamoto, ndipo Iye anati 'Zonsezi... Ichi chikhala chitsonyezo. Iwe udzabwera ndi anthu ndipo udzazera pa malo omwewanso!' Ndipo tsopano ndi uyotu Mulungu mu Lawi la Moto lomwelo monga ndinakuuzani kuti Iye anali m'menemo, ndi uyono akuwoneka pa phiri lija. Lero uneneri uwu wakwaniritsidwa. Uyu ali apayu kutsimikizira kuti zimene ndimakuwuzani zija ndi Choonadi."

Mulungu tipatseni amuna ena monga amenewo, amene ali okhulupirika ndi owona mtima ndi onena Choonadi, kuti Mulungu Wamphamvuzonse atsimikizire kuti Mawu Ake ali Choonadi! Iye adakali yemweyo dzulo lero ndi nthawi zonse. Angalephere bwanji kuchitanso? Iye analonjeza kuti adzatero.

Yoswa akanakhoza kunena chimodzi modzi pa tsiku limene anabwerera ku Kadesh-Barnea pamene anayenda ulendo wotero m'chipululu Iwo anali kukayikira dzikolo kuti lingakhale monga momwe Mulungu ananenera koma Mulungu anali atawauza iwo za dziko labwino; linali loyenderera mkaka ndi uchi. Ndipo Yoswa ndi Kalebi anali awiri okhawo amene anakhulupira pamene ena khumi anakayika. Pamene iwo anali kubwerera anatenga maphava a magerepi amene ankanyamulidwa ndi amuna awiri a mphamvu.

Yoswa ndi Kalebi akanakhoza kuyima pamenepo nati, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa!" Umboni wakuti dzikolo ndi labwino ndi uwu. Mukanazipeza kuti zinthu zoterozi mu Egypt?" Kunalibe malo oterowa. "Koma Lero Lembo ili lakwaniritsidwa!" Iye akanakhoza kunena kuti chinthu - chomwe iye anachinenera nati makoma a Yeriko adzagwa atatha kuguba mozungulira mzindawo Kasanu ndi Kawiri - masiku asanu awiri, Kasanu ndi Kawiri pa tsiku, lotsiriza. Ndipo pamene anazungulira kotsiriza, makoma anagwa! Yoswa akanakhoza kuyima nati, "Lero monga momwe Mtsogoleri Wamkulu wa gululi wa Ambuye anandiwuzira ine sabata lathalo kuti zidzatero, lero Lembo ili lakwanitsidwa! Makoma pamenepo anali atagweratu pansi. "Tiyeni, tiyeni tiwutenge; ndi wathu."

Lero Lembo ili lakwanitsidwa. Zodabwitsa kwambiri, momwe anthu a Mulungu akhala akuyimira zinthu zowona.

Israeli, pa mtsinje pamene iwo anatenga dzikolo, atawoloka. Anachita bwanji? Unali mwezi wa April; ndipo mitsinje itazaza madzi, chifukwa chisanu chinali kusungunuka m'mapiri a Yudeya. O, Mulungu anawoneka ngati mtsogoleri wosadziwa pakubwera ndi anthu mu mwezi wa April pamene Yordano anali wokhuta koposa nthawi zina zonse.

Nthawi zina... Ndikanakhoza kuyima apa ndikanakhala ndi nthawi kuti ndingokubenthulirani pang'ono. Nthawi zina mukhoza kugwidwa ndi cancer kapena matenda ena. Mukhoza kuganiza, "Chifukwanji ine Mkhristu ndikukhala wotere? Chifukwa chiyani kuti ndizingokhala wotere pamene ndiri Mkhristu?"

Nthawi zina Mulungu amalola zinthu kuti zide mwakuti siwungawone m'mbali kapena kwina kuli konse, ndi pamene Iye amadza nakupyoletsa, kuti ukhoze kunena kuti, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa, limene analonjeza kulichita."

Iye analola ana a chihebri kuti alowe mu ng'anjo yamoto. Iwo anati, "Mulungu wathu akhoza kutipulumutsa ife mu ng'anjo yamotoyi koma ngakhale atati asatero ife sitigwada kwa fano lanulo." Pamene anatuluka m'menemo - sananunkhe fungo la ng'anjo ayi, m'malo mwake, akanakhoza

kunena kwa iwo, aja kuti, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa."

Pamene Danieli anturuka mu linga mikango, iye akanakhoza kunena chimodzi modzi.

Yohane Mbatizi, patapita zaka 400 za chiphunzitso cha zipembedzo... Ndi zosadabwitsa kuti mpingo unali utasokonezeka nthawi imeneyo. Pamene iye anayamba kupezeka mu chipululu, ku Yordano, iye ankakhoza kuyima mphepete mwa mtsinje, momwe iye anali kuchitira, nati "Lero Lemba ili (Yesaya 40) lakwanitsidwa!"

Ndikhoza kuyima apa kuti ndikufotokozereni zimene wansembe wachikulire uja anandiwuza. Iye anati, "Mwana'nga, sunatsirize Uthenga uja."

Ndinati, "Yembekezani."

Iye anati, "Ukutanthawuza kuti anthu a chipentekoste sakumvetsa zimene zija?"

Ndinati, "Ayi."

Iye anati, "Ine ndikumvetsa." N'kukhala wansembe wa Katolika tsopano. Iye anati, "Chifukwa chiyani sukupitiriza?"

Ndinati, "Yembekezani."

Iye anati, "Mulungu Alemekezedwe, ine ndikumvetsa!"

Ndipo mwa kanthawi komweko Mzimu Woyera unagwera pa mlongo amene anali pa msonkhano umenewo, ndipo iye ananyamuka nayamba kulankhula ndi malilime achilendo napereka tanthawuzo la zomwe ine ndi wansembe timakambirana pa guwa paja! Mpingo wonse, pa malo ponsepo panangopokosera! Nkhani imeneyi inapitirira mpakana ku msonkhano wa Oral Roberts sabata lathali. Za momwe wansembe anali... ndipo Mzimu Woyera unawulula kupyolera mwa mzimayi (ndikukhulupira anali, mlongo wake) za zonse zimene zinkachitika pa guwa nawulula chimene ife tinkachibisa!

Nthawi imene tikukhalamoyi lero Lembo ili lakwaniritsidwa! Lero kuwala kwa usiku kwabwera, ndipo tikulephera

kukuwona.

Tawonani, Yohane anati, "Lero, ine ndine Liwu lofuwula m'chipululu, monga ananenera m'neneri Yesaya. Konzani njira ya Ambuye!"

Iwo sanamumvetsa iye, nati "O, iwe ndi Yesu - iwe ndi Khristu," Kani.

Iye anati, "Ine sindine Khristu." Iye anati, "Ine sindiri woyenera ngakhale kumasula zingwe za sapato Zake, koma" Iye anati, "Iye ali pakati panu pomwepo! Pakuti ankatsimikiza kuti Iye ali pamenepo. Iye anayenera kukhalapo m'masiku a Yohane chifukwa Mulungu anamuwuza iye kuti adzatsonyeza Mesiya kwa anthu.

Tsiku lina Mwamuna wachinyamata anadza kumalo omwewo ndipo Yohane anawona - monga Kuwala pamwambwa pa Iye (chizindikiro) ndipo anafuwula, "Onani Mwana wa Nkhosa wa Mulungu. Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu!"

Zoona, pa nthawi ya Pentekoste, ndi pomwe Petro anayima nabwereza Lembo la Yoweli 2:28, pamene anthu onse anali kuseka - anthu a nthawi imeneyo. Awa samatha kulankhula chilankhulidwe chawo; ankangobwebweta zina zake. Baibulo limati, "Malilime ogawanika." "Cloven amatanthauza lilime logawanika, osatha kunena kanthu, kumangobwebweta, kuthamanga mozungulira monga anthu olezera.

Ndipo iwo onse anati, "Anthu awa alezera; tawawonani. Taonani momwe akuchitira - momwe azimayi ndi azibambowo... azunguzika;" anatero magulu a zimpembedzo a nthawi imeneyo.

Petro anayima pakati pawo, nati, "Amuna ndi abale, inu amene mumakhala mu Yerusalemu ndi inu a ku Yudeya, chidziwike kwa inu kuti anthu awa sanalezere monga momwe inu mukuganizira, pakuti lino ndi ora lachitatu la tsiku, koma ichi ndi chija chimene chinalankhulidwa ndi mneneri Yoweli. 'Ndipo kudzachitika m'masiku otsiriza kuti, Ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa matupi onse.' Lero Lembo ili lakwanitsidwa. Ndithudi.

Luther anafika pa nthawi yake yoyenera. Wesley pa nthawi yoyeneranso. Pentekoste wabwerezanso pa nthawi yoyenera. Palibe chimene chiri chosokonezeka.

Tsopano, ine ndikukufunsani inu kuti mulingalire za mbadwo ndi nthawi imene tikukhalamo tsopano ndi Mawu olonjezedwa a masiku ano. Ngati anthu a m'mibadwo yina akanakhoza kunena kuti, "Lero Lembo ili... Lero Lembo ili..." nanga bwanji Lembo la lero? Ndi chiyani chimene chinalonjezeredwera masiku ano? IFE NDIYE TAYIMA POTANI! Ndi ora lanji limene tikukhalamo, pamene koloko ikugunda koloko ya sayansi ili maminiti atatu okha kuti ikwane pakati pa usiku?

Dziko lonse lagwidwa malungo; mpingo uli pa kama wa chivundi. Palibe amene akudziwa pamene wayima. Nthawi yanji ya tsiku? Nanga bwanji Malembo onena za tsiku limeneli?

Chikhalidwe cha mpingo - momwe mpingo ulili masiku ano... Pa dziko, ndale zochitika za m'dziko, zonse zangovundiratu. Ine si wa za ndale; ndine Mkhristu ndipo ndiribe mphamvu zolankhulira za ndale, koma ndangofuna kunena kuti mbali zonse zavunda basi.

Ine ndinaponya voti kamodzi; kwa Khristu. Ndiyenera kuwina. Mdierekezi anavota motsutsana nane, ndipo Khristu anandivotera ine. Zimatengera mbali imene nditi ndiponyere voti yanga. Ziribe kanthu dziko lizinena zimene likufuna, ine ndikukhulupirabe kuti Iye ali yemweyo dzulo lero ndi nthawi zonse! Iye atsimikizira. Salephera konse. Ndithudi-

Kuchuluka kwa milandu - kusokonezeka mitu kwa anyamata ndi atsikana. Taliwonani fuko, limene kale linali duwa la pa dziko lapansi. Ndi ulamuliro wathu wa demokarase umene unabadwa kale lija - Pakukhala Dziko Loyima palokha - chivomerezo cha kuyima pa tokha china sayinidwa, ndipo tinakhala ndi demokarase, ndipo makolo athu akale anachita zinthu zimenezi. Tinali ndi fuko lopambana; koma tsopano lavunda, lakwinyata ndiponso ndi logwedezeka ndi kutinso likutha, akuyesa kuwalipiritsa anthu misonkho ndi cholinga chakuti apeze ndalama zakuti atumize kwina

pofuna kugula ubwenzi ndi adani. Iwonsi akungozitayira pa nkhope pathu. Kunali Nkhondo yoyamba ya dziko lapansi, yachiwiri, ndipo tikupitirirabe kuyandikira ya chitatu. Ndithudi. Ndale ndi zovunda, zosokonezeka - zovunda mwa thunthu. Kungokhala chimodzimodzi chimene Mateyu 24 anati zidzachitika. "Mafuko adzaukirana ndi mafuko ena, ufumu ndi ufumu wina."

Chabwino, taonani chinanso: kukwera kwa kufufuza kwa sayansi. Tsopano, nthawi ina kungoti... Agogo anga amuna ankapita kukawaona agogo akazi mu ngolo yokokedwa ndi ng'ombe. Tsopano ndi ndege za jeti kapena mu mlengalenga-m'mwamba kwambiri. Ndi zapammwamba. Momwe ... Ndani ananena izi? Danieli 12:4 anati, "Nzeru zidzachuluka m'masiku otsiriza." Tikuwona nthawi imene tikukhalamoyi.

Taonani tsopano - kakhalidwe ka pa dziko, momwe sayansi iliri. Ndipo onaninso lero pa maphunziro momwe zikuchitikira - tsopano ichi musakane ayi, ndiri ndi zimene ndinadula mu nyuzi pepala - kuphunzitsa chigololo mu tchalitchi - mu ma sukulu a ana okulirapo, ophunzira amuna kufunsidwa kuchita chigololo ndi atsikana kuti awone ngati angathe kupeza amuna oyenera akazi otani pa dziko lapansi! Inde, wawa.

Bwanji ansembe athu? Usiku uno ine ndiri ndi gawo la pepala, yokamba za ku Los Angeles, California, kumene gulu la azibusa (alaliki a Baptist ndi Presbyterian) anatenga gulu la amuna ogonana ndi amuna anzawo (homosexuals) kuti iwowo adzachite nawo zimenezo, namati cholinga chawo ndi kuti potero awatembenuzire kwa Mulungu, pamene limenelo ndi limodzi mwa matemberero a nthawi yathuyino - Sodomu wina! Kotero ngakhale lamulo linawamanga iwo.

Tsopano tiri kuti? Kachitidwe kathu konse kavundiratu. Ndawona chiwonjezekero cha amuna kapena akazi omagonanawa kuti mu Amerika chinawonjezereka ndi 20% kapena 30% chaka chathachi. Taganizani za zimenezo! Mwamuna kukhala ndi mwamuna nzake, monga momwe ankachitira mu Sodomu.

Kuchuruka kwa mirandu - kusokonezeka kwa anyamata ndi

atsikana. Ndi nthawi yanji imene tikukhalamoyi? Lero Lembo ili la uneneri lakwanitsidwa.

Dziko la chipembezo, mpingo umene, mpingo wotulutsidwa (umene tikuwutcha wotulutsidwa), mu mbadwo wa mpingo wotsiriza uno, mbadwo wa chipentekoste - uli potani? Tiri mu mbadwo wa Laodikaya monga momwe malembo ananenera.

Lero anthu alekelera ziwongolero. Azimayi awo ali amariseche, amuna awo ali... ndi zonyansa kwambiri! Ena a iwo ndi okuti akwatira katatu kapena kanayi, kumakhala madikoni ndi utumiki wina otero. Alekelera ndipo abweretsa chivundi, chifukwa ayambitsa mabungwe amene akanamachitika ndi anthu aza dziko. Ndipo lero ali ndi zinyumba zabwino kusiyana ndi kale lonse. Malo ena a iwo anamangidwa ndi ndalama zokwana madola 50 miliyoni bwalo losonkhanirapo lokhalo - madola 50 miliyoni! - A Pentekoste amenewo! Poyamba anali ongosonkhana pa kakona zaka 25 zapitazo akumayimba nkhotcho zawo. Akuti, "Ife... chifukwa..." Malembo anati pa Chivumbulutso 3 kuti ndinu olemera. Akuti, "Ndine wolemera, ndikukhala ngati Mfumu Kazi, sindisowa kanthu." "Ndipo siukudziwa kuti ndiwe opanda pache, omvetsa chisoni, wosauka, wamaliseke, wakhungu" - ndipo siukudziwa ayi! Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu. Amen!

Amen amatanthauza zikhale motero. Sindikudzichita amen ndekha, koma ndikutanthawuza kuti ndikukhulupira kuti zimenezi ndi Choonadi. Lero Lembo ili lakwanitsidwa.

Mpingo wa Pentekoste uli mu chikhalidwe cha Laodikaya. O, amadumphabe nakuwa ndi kuchita izi ndi izi pamene akuyimba nyimbo. Nyimbo ikatha - kapena pamene nyimbo zikuyimbidwa ndi magaye ndiye nkumati zimenezo ndi nyimbo za Chikhristu - ndipo pamene atsiriza kuyimba ulemelero wa chipembedzo umathera pomwepo.

Ngati kuli kupembedza Mulungu kweni kweni, palibe malikhweru kapena mphamvu zokwanira pa dziko lapansi zimene zingathetse ulemelero wonse. Pamene ukuchokeradi kwa Mulungu sizimatengeranso nyimbo kuti ukhalepo; zimatsitsa Mzimu wa Mulungu; ndipo umakhazikika! Ndipo zoterozi anaziyiwala kale, chifukwa anawonjezera za

makono pa mphatso ya Mzimu Woyera - namati chitsonyezo cha Mzimu Woyera ndi kulankhula malilime, pamene ine ndinamva adierekezi ndi afiti akulankhala ndi malilime!

Mzimu Woyera ndi Mawu a Mulungu mwa inu umadziwika pakuvomerezana ndi Mawuwo. Ngati zisiyana ndi Mawu ndiye si Mzimu Woyera. Ngati muli ndi Mzimu Woyera ndiye kumakana Mawu ena a M'Baibulo, umenewo si Mzimu Woyera. Chimenechi ndicho chitsonyezo ngakhale mukukhulupira kapena ayi.

Taonani, chizindikiro china chachikulu. Ayuda ali mu dziko la kwawo, fuko lawo lawo, ndalama zawo zawo, membala wa bungwe la United Nations, ali ndi asiri - kali awo awo; ali ndi chiri chonse. Ali ku mudzi kwawo monga momwe Yesu anati, "Phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu. Ndi amenewotu, abwerera kwawo. Lero Lembo ili lakwanitsidwa.

Ayuda ali kwawo - Lero Lembo ili lakwanitsidwa. M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya - Lero Lembo ili (Mateyu 24) lakwanitsidwa. Dziko lasokonezeka (lonse limene), mafuko kudana ndi mafuko ena, zivomezi m'malo akuti akuti, zimphepo zowopsya zikudza ndi kugwedeza mafuko ndi zina zotero, ngozi zowopsya kuli konse - Lero Lembo ili lakwanitsidwa.

Tsopano, tawona za chikhalidwe cha m'dziko. Tawona pamene mpingo wachidziko - bungwe, madinomineshoni, tawona pamene ayima. Tikuwona pamene mafuko ali. Ndipo tikuwona kuti Lero Lembo ili lakwanitsidwa. Tsopano! Koma masiku ano kuyeneranso kudza Mbewu yopambana ya Chifumu ya Abrahamu. Ndi momwe ziti zichitikire, kupezeka Mkwatibwi Wachifumu wa Mwana wolonjezedwa wa Chifumu. Monga momwe ndinalankhulira usiku wathawu, siyikhala mbewu wamba ayi, ikhala Mbewu ya chifumu ya chikhulupiro cha chifumu cha ana a Chifumu a Abrahamu. Iyeyu apezeka pa masiku otsirizawa, mwa nthawi ndi malo a lonjezo amene anaperekedwa kwa iye malingana ndi Malaki 4 (Lembo lake). Kupezeka Uthenga umene uti ugwedeze mitima ya wanthu kuwabwezeretsa ku chikhulupiro cha atate awo atumwi.

Papezeka wina amene ati awonekere ndi mphamvu za Eliya - amene ati apezeke; munthu wokonda chipululu amene adzakhala ndi Uthenga umene uti udze kuchokera m'Mawu. Ndi nthawi yomwe tikukhalamoyi.

Kotero lingalirani. Tsopano, ndikufunseni pa nthawi ino, inu anthu akuno ku Jeffersonville chaka cha 1933, pamene Kuwala kwa uzimu kunatsika kuja ku mtsinje tsiku lija pamene ndinali kubatiza anthu 500 mu Dzina la Yesu Khristu (pamenepo ndinali m'nyamata wa zaka makumi awiri), Kodi Kuwala kuja kunali chiyani, Jeffersonville? Chinali chiyani kuja kuli msewu wotchedwa Spring Street, pamene a nyuzi pepala Ya Courier Journal (Ndikuganiza inali Louisville Herald) momwe analemba, ndipo zinakalembedwanso ndi a Associated Press, mpakana ku Canada. Dr. Lee Vayle anandiwonetsa gawo la pepala ya ku Canada'yo m'chaka cha 1933!

Pamene ndinali kubatiza munthu wa nambala 17 panadza Mboni imeneyi (monga mukudziwa nkhani yonse), ndipo pamene ndinali pamenepo kubatiza munthu wa nambala 17 yu, Kuwala kunatsika kuchokera kumwamba, kunawala pamenepo monga nyenyezi yoti yagwa kuchokera kumwamba Liwu linati, "Monga Yohane Mbatizi anatumidwa ndi Uthenga wotsogolera kudza koyamba kwa Khristu, Uthenga wako utsogolera kudza Kwake kwa Iye kwa chiwiri ku dziko lapansi." Lero Lembo ili lakwanitsidwa! Zikomo, Ambuye.

Masiko ano... Mulungu analonjezeratu. Chinachitika ndi chiyani? Masiku ano anthu akudziwa nkhaniyi pa dziko lonse lapansi. Ndipo pamene Mulungu anatsika nanena nane (pamene ndinali kamwana) mu chitsamba choyaka kapena nditi pakathengo mu moto wa Lawi la Moto - konkuno kwa a Wathen ku Utica pike, pamene ndinali kuchokera kokatunga madzi cha ku barani kuja. Mukudziwa kuti ndikunena zowona.

Iye anati, "Usadzasute fodya, kapena kumwa mowa, kapena kuyipitsa thupi lako ndi akazi, pakuti pali ntchito imene udzandigwirira ukadzakula."

Ine ndikuchitira umboni uwu pa kuti ndi Choonadi cha zimene ndinaziwona! Ndipo Mulungu monga momwe Iye

anachitira ndi Mose, anadzalankhulanso pamaso pa msonkhano wa anthu Kumtsinje Kuja nati, "ICHI NDI CHOONADI!" Lero Lembo ili lakwanitsidwa pakati pathu!

Tapenyani zimene Iye ananena za kudziwa zobisika za m'mitima ya anthu ndi momwe ziti zizidzachitikira kuchokera pamene ndinkayika dzanja langa pa iwo ndi kumadziwa zinsinsi za m'mitima yawo. Lero Lembo ili lakwanitsidwa pa maso pathu pomwe! Malonjezo awa amene anaperekedwa.

Tawonani, malonjezo onsewa akwaniritsidwa ndi kutsimikiziridwa ndi Mulungu amene anadilonjezayo. Tawonani, chimene chiri chopachikidwa mu nyumba yosungiramo zinthu zotchuka ku Washington, D.C. usiku uno, chithunzi cha Mngelo wa Ambuye. Monga momwe George J. Lacy, mkulu wa mateketefi a F.B.I. ofufuza za kudinda kwa zala ndi mabukhu a Boma la America, iyeyu anafufuza napima chithunzichi ku Houston, Texas nati "Ichi ndi chithunzi chokha chimene chapezeka pa dziko lonse lapansi chimene chiri cha Uzimu." Iyeyu anayenera kudziwa; iye ndi kaswiri amene alipo pa dziko lonse lapansi pa ntchito yofufuzayi.

Tawonani ndi ichotu chimene chiri chopachikidwa kuvomereza kuti ndi Choonadi, Lawi la Moto lomwe linatsogolera Aisraeli mu chipululu lija. Tikuliwonanso lero chimodzimodzi momwe Mulungu anadzizindikiritsira kuti ali pakati pa anthu amene anatuluka ku Egypt! Ndi ndani ameneyu? Lero Lembo ili lakwanitsidwa. Inu mukudziwa Uthenga umene Iye anapereka.

Tawonani masomphenya a ku Tucson zaka zitatu zapitazo. Pamene ndinayima pa msewu, pamenepo patatha zaka zisanu pomwe Iye anati, "Tsiku limene a mzinda adzakhome chikhomo pa chipata cha nyumba yako, udzachoke kuno kupita cha ku mazulo." Abale anga a mu kachisi uyu amene ali pano akudziwa kuti zimenezi ndi zowona - za nthawi imeneyo. Ndi momwemo.

Ndipo tsiku limenelo a bambo a Goyne ndi wenanso anafika pamtunda apa nakhoma chikhomo, ine ndinati kwa mkazi wanga, "Pali china chake chokhuzana ndi chikhomochi."

Iye anati, "Ndi Chiyani?"

Ndipo ndinalowa, kukayang'ana mu ka bukhu kanga; ndinazipeza m'menemo! Ndipo m'mawa mwake pa 10 koloko, nditakhala mu chipinda changa pafupifupi 10 koloko. Mngelo wa Ambuye anadza nati, "Pita ku Tuscon. Udzikakhala mbali ya kumpoto cha kum'mawa kwa Tuscon ndipo kumeneko adzadza Angelo asanu ndi awiri mwa gulu ndipo kudza kwawo kudzagwedeza dziko lapansi kuchokera pamene iwe udzakhala uli." Ndipo anati, "Ukawuzidwa zina zonse komweko."

Ndi angati amene akukumbukira zimenezi pano, panatenga nthawi kuti zichitike? Pali abale pano mu nyumba ino usiku uno amene anayima pomwepo pamene zinkachitika, ndipo ndinawuzidwano kuti zisindikizo zisanu ndi ziwiri za zinsinsi zobisika za mu Baibulo lonse zidzawululidwa ndi kukwaniritsa Chivumbulutso 10, kuti ndi Uthenga wa Mngelo wa Chisanu ndi Chiwiri zinthu izi zidzachitika! Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu! Lero Lembo ili lakwanitsidwa.

Chaka chatha ndinayima pa malo omwewo (Bambo a Wood awa ndi ine) pamene tinali kukwera phiri, pochita - ngati kukalira chifukwa choti akazi awo anali akudwala. Mzimu Woyera anati, "Tola mwala uli apowo, nuwuponye m'mwamba; ndipo pamene ukugwa pansi unene kuti, 'ATERO AMBUYE!' Chiweruzo chikhuza dziko lapansi. Umuwuze uyo kuti awona dzanja la Mulungu pa naora ochepa."

Ine ndinamuwuza Mr. Wood (amene tiri nawo usiku uno) ndipo ndikuganiza anthu ena asanu ndi atatu kapena khumi - kapena khumi ndi asanu analipo nthawi imeneyo, pamene zinali kuchitika m'mawa mwake, pamene Ambuye anadza mu kamvuluvulu nang'amba pa phiri pozungulira ife, ndi kudula nsonga za mitengo, ndipo kunachitika ngati kuphulika katatu ndipo anati, "Chiweruzo chikupita ku gombe la Kumazulo!"

Patangopita masiku awiri Alaska anali pafupi kumezedwa mu nthaka! Ndipo kuyambira pamenepo kuntunda kapena kumusi kwa gombelo kwakhala kukuphulika Chiweruzo cha Mulungu monga momwe 'anandiwonetsera mwauzimu!'

Pali katani la Chitsulo, pali Katani la Nsungwi, ndipo pali Katani la Tchimo! Chitukuko chayenda ndi dzuwa; chimodzimodzinso Uthenga. Ukuchokera Kum'mawa ndipo wapita ku mazulo momwe dzuwa limapitira ndipo tsopano uli ku gombe la kumadzulo. Siwungapitirirenso apa; ukati upitirire, ndiye kuti ubwereranso Kum'mawa.

Mneneri anati, "Kudzakhala tsiku limene silidzatchedwa usiku kapena masana," - tsiku lachimbuuzi, kwa mvula pambiri ndi chifunkha, kungotha - kungodziwa kujowina mpingo kapena kulembetsa dzina lako m'bukhu. Koma kudzakhala Kuwala-Kuwala mu nthawi ya mazulo. Lero Lembo ili lakwanitsidwa!

Lomwelo... Dzuwa (S-U-N) lomwe limatuluka kum'mawa ndi dzuwa lomwe limakalowanso kumadzulo. Ndiponso Mwana (S-O-N) wa Mulungu amene anadza ku m'mawa nadzitsimikizira yekha ngati Mulungu amene anasandulika thupi, ndi Mwana wa Mulungu yemweyo ku chigawo cha kumadzulo kuno, amene akudziwonetsera Yekha pakati pa mpingo usiku uno - yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse! Kuwala kwa mazulo kwa Mwana kwafika. Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso pathu.

Tiri kuti ife nanga mu mbumba ya Abrahamu'yi? Tiri kuti pa nthawi ya kayimidwe kopambanayi, nthawi yopambana imene tikukhalamoyi? Maso mphenya onse akwanitsidwa. Bwanji pamene kamlaliki kanzathu, mbale wathu ku mpingo woyanjana nafe (Junior Jackson), anadza chothamanga kwa ife usiku wina (kumene ndinali) nati, "Ndinali ndi loto, Mbale Branham, limene likundisautsa. Ndinawona abale atasonkhana pa phiri." Nati, "Pa phiri limeneli, inu munali kuphunzitsa zolembedwa zimene zinali, pamenepo, zimawoneka ngati zolemba zimene anachita kugoba pa thanthwe. Pamene munatsiriza zimenezo - zonsezo mutatsiriza munatiwuza ife, kuti, 'Yandikirani' ndipo ife tonse tinasonkhana." Nati, "Inu munafikira dzanja lanu kwina kwake ndipo kukuwoneka ngati munatenga, chokhala ngati chikwanje chimene muna yengula nacho pamwamba pa ka (piramidi) kaphiri aka. Ndipo mutatero," anati, "unaoneka mwala woyera wopanda zolemba pa iwo, Ndipo inu munatiwuza kuti tiziyang'ana pa mwalawo. Ndipo inu nonse - ife tonse tinayamba kuyang'ana." Nati, "Ine ndinatukula mutu wanga, ndipo ndinawona kuti inu mukupita cha ku-

mazulo mofulumira ndithu, cha kolowa dzuwa." Ndi angati amene akukumbukira izi?

Ndipo ine ndinayima pamene paja pang'ono mpaka pomwe Mzimu Woyera unandiwululira izi. Ndinati, "Baibulo lonse, zonse zimene zawululidwa kwa munthu kupyolera mu chilungamitso, chiyeretso, ubatizo wa Mzimu Woyera ubatizo mu Dzina la Yesu, ndi zonse izi zimene zawululidwa, koma zinsinsi zimene zabitsidwa mkati, chifukwa Baibulo linali lomatidwa ndi zomatira zisanu ndi ziwiri. Ndiyenera kupita kukafufuza kumeneko za zimenezi."

M'mawa umenewo pamene Angelo asanu ndi awiri anadza nachititsa bingu ndipo miyala inawulukira konse konse, Angelo asanu ndi awiri'wo pamenepo anati, "Bwerera ku Jeffersonville kuchoka kumene wachokera, pakuti zomatira zisanu ndi ziwiri za Zinsinsi zisanu ndi ziwiri zikamatulidwa."

Pano lero, timvetsa, 'Mbewu ya Njoka' pa masiku ochepa, ngati Mulungu alola, timvetsa kulongosola kweni kweni kwa 'Chikwati ndi Kulekana' ndi zina zonsezi zimene Mulungu anatsegula, chomatira chiri chonse, zinsinsi, kuyambira pa chiyambi cha dziko lapansi, ndipo ife takhala pa phwando la Mulungu pamene Iye ali pakati pathu ndi madalitso Ake. Izo ndi zowona. Lero Lembo ili...

A Life magazine analemba nkhani ya 'Kuwala kodabwitsa kwa maonekedwe ozungulira kunali kuyandama ku Tucson ndi Phoenix" - mwa njira imene ndinakuwuzani pafupifupi chaka chimodzi chapitacho zisana chitike, momwe zidzawonekere - ngati kabwalo kosongoka mbali imodzi. Chithunzi chake tiri nacho mu tchalitchi muno cha uko. Inu amene munagula magazine, m'menemo chilipo. Mwawona momwe chinawonekera ndendende. Akuti chinali kutalikira kwake kupita m'mwamba ma mailosi 27 koma utali wake mamailosi 30 chopingasa. Anthu sakumvetsabe chimene chinachitika. Chinawonekera modabwitsa ndipo chinazimanso modabwitsa.

Ndipo Mbale Fred Sothman, M'bale Gene Norman ndi ine tinali titayima pamenepo, anthu atatu ochitira umboni, monga momwe zinachitikira pamwamba pa phiri - Petro, Yakobo ndi Yohane. Iwo anali mboni; anali pamenepo

namapenya pamene zinali kuchitika. Ndi ichinso, chimene chinayandama mu mlengalenga kutali kumene kulibe chinyezi, mpweya wonyowa, kulibe chakuti chingapange - mtambo. Nanga chinapezeka bwanji pamenepo? Iwo anali Angelo a Mulungu pamene anali akubwerera atatha kupereka Uthenga wawo. Lero uneneri wawo wakwaniritsidwa pakati pathu! Lero Lembo ili lakwanitsidwa.

Yang'anani. Zimatiro zisanu ndi ziwiri zamatulidwa, kamvuluvulu wagunda gombe la kumazulo. Tsopano, zisakupiteni monga momwe anachitira m'mbuyomu. Tsopano,tiyeni timvetse zimene zikuchitika masiku athu ano.

Kodi Malembo akuti chiyani za masiku ano amene tikukhalamo? Yesu polankhula... sindikhala ndi nthawi yofotokoza zonse, koma ndikufuna kufotokoza chinthu chimodzichi ndisanatsirize. Yesu anati pa Luka chaputala 17 vesi 30 - Yesu Khristu, Mawu Ake omwe (kodi mungakhulupire zimenezo?) - Yesu Khristu, Mawu Mwini wake amene anasanduka thupi, analankhula nafotokoza momwe Mawu adzakhalire pa nthawi yotsiriza, chimene chidzakhala chizindikiro cha chitsiriziro cha dziko lapansi. Iye anawawuza kuti mafuko adzawukirana ndi mafuko wena, komanso Iye anati, "Monga momwe kunali m'masiku a Sodomu kudzakhala chimodzimodzinso pamene Mwana wa munthu adzawululidwa."

Tsopano, pamene Yesu adza pa dziko lapansi Iye adza mwa mayina atatu a Mwana: Mwana wa munthu (chimene chimatanthauza m'neneri), Mwana wa Mulungu, ndi Mwana wa Davide. Tsopano Iye anakhala pa dziko lapansi, sanadzitchule yekha ngati Mwana wa Mulungu. Iye anati, "Ndine Mwana wa Munthu." Yehova Mwini wake anamutcha Ezekieli amene anali m'neneri "Mwana wa munthu," chifukwa Iye anayenera kudzadza kudzakwaniritsa Lembo la uneneri! Mose anati, "Ambuye Mulungu wanu adzakupatsani Mneneri monga ine." Icho ndi chifukwa chimene Iye sakanakhala Mwana wa Mulungu pa nthawi imeneyo, chifukwa Iye anali Mwana wa Munthu! Mawu anadza kwa mneneri kuti Iye anali Mwana wa Munthu! Mawu anadza kwa mneneri kuti Iye anali chidzalo cha Mawu! Mwana wa munthu, M'neneri wamkulu, osatinso Mneneri wamkulu, koma Mulungu Mneneri! Chidzalo cha umulungu chinali mu thupi lake, kotero Iye anali Mwana wa munthu.

Tsopano kwa zaka zikwi ziwiri Iye wakhala akudziwika kwa ife monga Mwana wa Mulungu, Mzimu. Ndipo mu mileniyamu iye adzakhala Mwana Wa Davide pa Mpando wachifumu. Ife tonse tikudziwa zimenezo, amene timakhulupira Malembo.

Tsopano Yesu anati potsiriza pa mbadwo wa mpingo umene tikukhalamo uno, kuti Mwana wa munthu adzawululidwanso mofanana ndi momwe zinali nthawi ya Sodomu. Onani momwe zikugwirizanira ndi umo zinali poyamba. Iye anati, "Monga zinali m'masiku amenewo, poyamba, masiku a Nowa. Pamene iwo anali kudya, kumwa kukwatira ndi kukwatiwa." Ndiye Iye anakambaponso kenako za Mwana wa Munthu mu nthawi ya Sodomu pamene Iye ali kuchita ndi anthu a mitundu. Kujaku Iye anawamiza iwo m'madzi ngati chiweruzo chawo. Kuno kwa amitundu, anawawotcha iwo onse pa tsiku lija mu Sodomu. Ndi motero; dziko la Amitundu linawotchedwa pamenepo.

Kudzakhalanso chimodzi modzi pamene Mwana wa munthu adzaululidwa. Yesu anali kuwerenga Genesis 23 yemwe tikuwerenga ifeyo, pamene anawerenga za Sodomu.

Tsopano, ife tikuvomereza za chikhalidwe chimene chinanenedwa - za - chikhalidwe cha dziko la Sodomu, Sodomu - khalidwe la Sodomu. Aliyense akhoza kunena kuti, 'Amen' pa chimenecho; tikukhulupira ichi. Chabwino, khalidwe lauzimu la Laodikaya, mpingo wamba, tikhozanso kunena kuti, 'Amen' pa chimenechi, ndi kuvomereza zizindikiro zawo. Ife tikudziwa kuti zizindikiro zonse ziripo; mpingo uno ndi wa Loadikaya tikudziwa zimenezo. Tikudziwa dziko liri mu khalidwe la Sodomu. Si choncho? Tikhoza kuvomereza zimenezo. Nanga bwanji chizindikiro cha Abrahamu, amene anali akuyembekereza mwana wa lonjezo? Uyo anali wina wapadera. Kumbukirani, iwo ku Sodomu kuja, anali ndi atumiki awo. Ndipo Abrahamu anali ndi Mtumiki wake. Abrahamu anali kuyembekezera tsiku ndi tsiku - pa chinthu chokhala ngati sichingachitike - Sarah wa zaka nayinte ndi iye wa zaka handirede. Malingana ndi lonjezo la Mulungu iye anali kuyembekezerabe. Pakati pa kutsutsidwa konse iye anayembekezera mwanayo. Ndi momwe wokhulupira wowona akuyembekezera Mwana wa lonjezoyo kuti adzenso.

Tawonani, mwanayo asanadze, panali chizindikiro chimene chinaperekedwa kwa iye Kodi chizindikiro cha kudza kwa Mwana sindicho pamene kudzawululidwe kwa Mbewu ya chifumu ya Abrahamu amene akuyembekezera Mwana wa Chifumuyo chimodzi modzi momwe Zinaliri kwa atate Abrahamu poyembekezera mwana mwa thupi? Si choncho? Yesu anati apa pa Luka 17:30, nthawi imeneyi isanadze, kuti Mwana wa munthu adzawululidwa monga momwe anachitira m'masiku a Sodomu, chisanachitike. Tsopano, ife tikufuna Chizindikirocho.

Tsopano tiyeni titenge...?...chikhalidwe cha nthawiyo monga kunaliri mu Sodomu. Tawonani, onse analowelera mu dziko la Sodomu. Ndikuganiza za munthu wotsogolera za kupanga ma kanema pamene anawonetsa chithunzi cha momwe Sodomu analiri posachedwapa, ine ndinakawonenera nawo. Mutangochiwona palibenso chimene munganene. Chinalidi chithunzi chabwino cha America lero - ku Hollywood, chimodzi modzi, kavalidwe kofanana ndi zina zonse zimene iwo anali kuchita nthawi imeneyo, maphwando aakulu a mowa ndi zina zonse - gulu la anthu achipembezo, zimene mukuzitcha zipembezo.

Tawonani, Sodomu anali ndi mboni. Iyeyu anali munthu wotchedwa Loti, amene anali mzukulu wa - Abraham. Tsopano, Abrahamu'tu sanakakhale nawo ku Sodomu. Iye ndi gulu lake - anali ndi gulu lalikulu ndithu, lokhoza kumenyana ndi mafumu khumi ndi awiri pamodzi ndi atsirikali awo; kotero anali ndi gulu lalikuludi. Ndipo iye anali atakhala pa nthunzi wa mtengo, pamene kunadza anthu atatu kwa iye. Awiri a iwo anapitirira ku Sodomu kukalalikira Uthenga kwa iwo anatuluka - kwa Loti. Si choncho? Koma m'modzi anatsala ndi Abrahamu. Tawonani, m'modzi amene anatsala ndi Abrahamu anali Mulungu Mwini; awiri enawo anali Angelo Otumikira.

Tsopano mu Sodomu sanachitemo zozizwitsa anagowachititsa anthu khungu, ndipo kulalikira kwa Uthenga kumawachititsa anthu khungu.

Tsopano yang'anani momwe zinthu zinaliri masiku amenewo. Pali mpingo wamba. Nthawi zonse patatu (monga momwe ndinanenera usiku wathawu) ndi momwe-momwe

Mulungu amayimiriridwa. Panali Asodomu, Aloti, ndi Abrahamu. Ziri chimodzi modzi usiku uno, dziko liri mofanana chotero!

Ndiloreni ndikufuseni china chake. Tawonani momwe zinthu zinalirino. Abrahamu anamutcha munthu uyu, Elohim. Liwu la chiheberi lakuti Elohim limatanthauza Iye amene ali Mwini wa zonse, Iye amene ali wa Muyaya - Elohim, Mulungu Mwiniwake.

Pachiyambi... Genesis 1 anati, "Pachiyambi, Mulungu..." Tatengani Liwu la Chihebri'lo - Liwu la chigriki kani, Pachiyambi Mulungu analenga Kumwamba ndi dziko lapansi."

Izi ziri apazi, Genesis, payenera kukhala pa 22 Iye anati ...?...Tiyambe kapena cha pa 20... Iye anati... Ndipo anamutcha Mwamuna uyu Elohim. Chifukwa chiyani anatero? Mulungu anayimiriridwa mu Khungu la munthu, amene anakhala pansi ndi Abrahamu nadya sangweji ya nyama ya ng'ombe, namwako mkaka, nadya mkate - Mulungu Mwini - ndipo anasowa pamaso pa Abrahamu! Koma Iye anamupatsa iye Chizindikiro. Tawonani, ndipo chizindikiro chimenecho chinali chakuti Iye anali atalodzetsa msana wake ku chihema. Ndipo kumbukirani Abrahamu, dzina lake linali Abram panangopita masiku angapo okha, ndi Sarah anali Sarra poyambapo S-A-R-R-A, kenako S-A-R-A-H ndi A-B-R-A-M nakhala A-B-R-A-H-A-M. Abraham amatanthauza atate wa mafuko.

Tsopano, onetsetsani apa, ndipo tiwona kakhalidwe ka nthawi imene tikukhalamoyi, monga momwe Yesu anatiwuza kuti tiyang'anire kakhalidwe koteroko. Tawona zambiri za zonsezi kale; tsopano tiyeni tiwone za Mbewu Yachifumu, kuti khalidwe lake liyenera kukhala lotani.

Tsono, Mwamuna uja anati, "Abraham, ali kuti mkazi wako, Sarah?"

Ndipo Abraham anati, "Iye ali mu hema kumbuyo kwanuko."

Tsopano, Iyeyu anali asanamuwoneko Sarah. Nanga anadziwa bwanji kuti dzina la uyunso linali Abraham? Anadziwa bwanji dzina la mkaziyo kuti anali S-A-R-A-H? "Abraham,

ali kuti mkazi wako, Sarah?"

Anati, "Ali mu hema kumbuyo Kwanuko.

Ndipo Iye anati, "Ine (ine peresonalo poronauni) - Ine ndidzakuchezetsani inu monga mwa lonjezo. Mkazi wako alandira mwana uja. Iwe wandidalira Ine, tsopano ndichititsa kuti panganoli likwaniritsike."

Ndipo Sarah mu hema kumbuyoko (anali kumvetsera, kapena kutcherera khutu, muli monse momwe munganenere), akumvetsera mu hema uja, ndipo anati - anaseka cha mumtima nati, "tsopano ine, mkhalamba yaikazi momwe ndilirimu, ndingasangalatsidwe ndi mbuye wangayu pamene iyenso ali wokalamba, pamene tsopano ali ndi zaka handirede."

Ndipo Mwamunayo M-W-A-M-U-N-A, amene anali pamenepo mu thupi la munthu, namwa ndi kudya monga munthu wamba aliyense zovala zake ziri ndi fumbi, ndi mapazi Akenso anali ndi fumbi ndipo Abrahamu anamusambitsa - Mulungu, Mwiniwake, anayang'ana uku ndi uku nati," Chifukwa chiyani Sarah akuseka mu hema kumbuyoku pamene ndikukuwuza izi?"

Iye anadziwa, ankakhoza kudziwa malingaliro a Sarah mu hema kumbuyo kwa Iye. Si chonco?

Tsopano pamene Mbewu yachifumu ya Abraham inadza pa dziko lapansi, inawonetsa Chizindikiro chotani? (Mwana wa Munthu). Simon anadza kwa Iye tsiku lina, Andreya ndi yemwe anakamutenga. Iye anati, "Dzina lako iwe ndi Simon; ndiwe mwana wa Yona." Iye anati... Mwaona, chokhacho chinamupangitsa iye kukhala wokhulupira.

Filipo anapita kwina nakapeza Nataniyeli, anadza nati, "Tiye ukawone Mwamuna; amene ife tamupeza - ife tamupeza: Yesu wa ku Nazareti, mwana wa Yosefe."

Iye anati, "Dikira kaye pang'ono. Kodi kanthu kabwino kangachokera pa zinthu zongotengeka zoterozo?"

Iye anati, "Tiye ukawone."

Kotero pamene Filipo anadza Pamaso pa Yesu ndi Nataniyeli, Yesu anayang'ana iye nati, "Onani Muisraeli amene mwa iye mulibe chinyengo."

Iye anati, "Rabbi, munandidziwa liti ine?"

Iye anati, "Filipo asanakuyitane iwe, pamene unali pansi pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe."

Iye anati, "Rabbi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu! Inu ndi Mfumu Ya Israeli!"

Pamene mwana wa mkazi uja anadza pa Chitsime, mu chikhalidwe cha chiwerewere, (zochitika mwina mwa njira yotere) Kudzatunga madzi, Yesu anali atatumiza ophunzira Ake Kumudzi kukagula zitumbuwa." Ndipo pamene anadza kudzatunga madzi, Iye anati, "Ndipatseko Ine Madzi akumwa, mzimayi."

Iye anati, "Si mwambo wake kuti Inu mutero kwa ine. Ndife osankhana kuno. Tsopano inu Muyuda mulibe chokuyanjanitsani ndi ife Asamariya; ife tiribe chochita ndi inunso."

Iye anati, "Koma mayi inu, mukadaziwa amene mukulankhula naye inuyo mukanandipempha Ine madzi akumwa. Ine ndikanakupatsani madzi kuti musamadzenso kuno kumadzatunga."

Iye anadziwa khalidwe lake la uyu momwe amakhalira. Anati, "Pita ukamutenge mwamuna wako adze kuno."

Nayankha, "Ine ndiribe mwamuna aliyense."

Iye anati, "Iwe wanena zowona. Iwe unali ndi amuna asanu ndipo amene ukukhala naye tsopano siwakonso."

Nayankha kuti, "Bambo inu, Ine ndawona kuti inu ndi m'neneri! Ife tikudziwa kuti pamene Mesiya abwera adzatiwonetsa ife zinthu zonsezi!"

Yesu anati, "Ine ndi Iyeyo!"

Kungotero mkaziyo anathamangira ku mudzi nati, "Idzani

mudzawone Munthu amene wandiwuza ine zimene ndimachita. Kodi ameneyu si Mesiya yemwe?"

Tapenyani, Iye anakhoza kuchita zomwezo pamaso pa Ayuda ndi Asamariya koma osati kwa Amitundu. Amitundu, anthu ife, tinali achikunja mu masiku amenewo (mafuko ena), tikuyenda, titaberekera zibonga, kupembeza mafano; ife sitimayembekezera Mesiya. Iye anangowonekera kwa iwo amene amamuyembekezera Iye, ndipo ife tikuyenera kumayembekezera Iye, tsopano! Koma iwo amene akuti akumuyembekezera Iye, Mpingo womwe, pamene akuwona zimenezo zikuchitika, akumati, "Ameneyu ndi m'diyerekezi, ndi wolota mwa masenga Belezebule!"

Ndipo Yesu anati chimo loterolo linakhululukidwa kwa iwo chifukwa Iye anali asanafe. Koma anati tsiku lina Mzimu Woyera adzabwera ndi kudzachita zomwe zomwezi ndipo kungolankhula liwu limodzi motsutsana naye basi simudzakhululukidwa. Zimenezo ndi za tsiku lino, pamene Liwu liri lonse liyenera kumangirizana ndi anzake. Ingolankhulani liwu limodzi motsutsana naye, simudzakhululukiridwa mu dziko ili kapena mu dziko liri nkudzalo.

Imeneyo inali Mbewu Yachifumu ya Abrahamu. Ndipo pano Mbewu Yachifumu ya Abrahamu'yo (imene ikudza chifukwa cha kufanana kwa zochita za Mwamuna uja amene anakhala pajapa ndi Abraham) idza kudzatsimikizira kuti anali Mulungu wa lonjezo yemweyo mu tsiku linonso, monga kunali m'masiku a Sodomu, kudzateronso pa kudza kwa Mwana wa Munthu, pamene Iye adzadziwulula Yekha monga Mwana wa munthu! Amen! Lero Lembo ili lakwanitsidwa.

Tawonani lero momwe zinthu ziliri. Tawonani Mpingo kumene Mwana wa Mulungu... Taliwonani tsiku la kuwala kochepa; tawonani uneneri wonse. Tsopano, Chinthu chachilendo - alendo athu ayenera kukhalapo tsopano, ngati kakhalidwe kake kayenera kufanana ndi ka Sodomu.

Panali atatu amene anadza -- anthu atatu apadera amene anatumidwa kuchokera Kumwamba, ife tonse tivomereza chimenecho - anthu atatu; M'modzi anasala ndi Abraham. Onsewo anayambira pamodzi, koma Mmodzi anasala ndi Abraham ndipo ena onsewo anapitirira napita ku Sodomu.

Si choncho? Ndipo Abraham anali atasintha dzina, kusiya la Abram nakhala Abraham. Zoona? Palibe nthawi ina mu mbiri ya dziko -- pamene nthawi ina mu mbiri ya dziko -- pamene mpingo pa dziko lonse lapansi unakhala ndi mlaliki wofalitsa Uthenga amene anali ndi dzina lotsiriza ndi H-a-m kupatula masiku ano -- Billy G-R-A-H-A-M. Si choncho? G-R-A-H-A-M -- Malembo asanu ndi limodzi A-B-R-A-H-A-M ndi malemba asanu ndi awiri, Koma G-R-A-H-A-M ndi malemba asanu ndi limodzi, amene ali munthu wa mu dziko -- munthu. Mwaona?

Tawonani amene afika kumeneko lero, ndi atumiki amene-wa chokera Kumwamba. Kodi aliponso munthu pa dziko la pansi amene walalikira za, kulapa momveka koposa Billy Graham? Aliponso kodi munthu amene amakoka anthu koposa Billy Graham? Sipanakhalenso munthu wotere wokhuza dziko lonse lapansi. Eee, kunali a Billy Sunday ndi wena wotero kuno ku America, Koma Billy Graham amadziwika ku dziko lonse lapansi. Mwawona kumene iye akuyitanira? -- kutuluka mu Sodomu! Ndipo iye ali ndi nzake amene akutumikira pakati pa mpingo wa chi Pentekoste -- ndiye Oral Roberts.

Koma bwanji gulu Losankhidwa? Ali ndi Chitsonyezo chotani choti achiwone? Ayenera kukhala ndi chiyani? Haleluya! "Kudzakhala Kuwala nthawi ya mazulo!" Lero Lembo ili lakwanitsidwa! Lero lonjezo la Mulungu lakwanitsidwa. Ife tikudziwa chimenecho kuti ndi Choonadi. Iye ali pano usiku uno monga Iye anali nthawi ijayo.

Tsopano, kuti tilalikirepo... Monga ine ndinanenera poyamba paja, ngati ulalikira chiri chonse ndipo ndi Choonadi cha Uthenga, Mulungu amakhala wokakamizika kutsimikizira chimenecho. Si choncho? Tsopano ngati ziri motero, kuyenera kuti Mulungu amene ananenera, kuyenera kuti Mulungu amene ali Mulungu wa Mawu adze poyera natsimikizire kuti Iye anakalibe Mulungu!

Monga momwe Eliya anapita ku phiri namayang'anitsitsa -- Elisha anapita namayang'anitsitsa Eliya, iye anati, "Ine ndikufuna magawo awiri." Ndipo chovala chimene chinali pa Eliya chinagwera chovalacho namenya pa mtsinje nati, "Ali kuti Mulungu wa Eliya?" ndipo chomwe chinachitika kwa Eliya, chinachitikanso kwa Elisha. Ndipo Uthenga

wofanana, mphamvu zofanana, Mwana wa Munthu yemweyo amene anali dzulo, ali yemweyo lero, ndipo adzakhala ku nthawi zonse! Ahebri 13:8. Kodi inu mukukhulupira vesi limeneli?

Tsopano, ine ndikufunsani. Ine sindingakhale Iye koma Iye yo ali pano. Ife ndi zotengera chabe. Ena mwa inu uko amene muli odwala ndi ozunzidwa (amene mukudziwa) kuti ine sindikukudziwani inuyo, tiyeni timulole Mulungu adziwe, ngati ine ndingadzichepetse ndekha kokwana...), inuyo pempherani ndi kufunsa Mulungu.

Sindikuchita kungoganizira mopeka... Palibe ali yense amene walandira khadi la osowa kupempherereredwa muno, alipo ngati? Ayi, Ine sindiku... Sitinapereke makadi kwa osowa kupempherereredwa. Tingokhala ndi msonkhano wa mapemphero - kapena machiritso a odwala ku kachisi. Koma inu pempherani, ndipo inuyo mukudziwa kuti ine ndi mlendo kwa inu. Mukuwona... Inu mukundidziwa ine, Jeffersonville! Ine sindikufuna anthu aku Jeffersonville kuno kuti atero; ine ndikufuna anthu akutali kwina. Tiwone ngati Mulungu amawululabe. Tiwone ngati ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse.

Chitani monga kamzimayi kaja. Yesu anali kupyola pamenepo ndipo uyu anati, "Ine ndikumukhulupira Munthu ameneyu." Anali ndi nthenda ya magazi nati, "Ngati nditangogwira mphonje ya chovala chake ndikukhulupira kuti ndichira." Si choncho? Chifukwa cha chikhulupiriro chake, tsiku limenelo Lembo linakwaniritsidwa. Iye ana manga mitima yosweka, 'Ndikachiritse odwala ndi opunduka.' Pamene mkaziyo anakhuza chovala Chake nayenda nakakhala pansi, Iye anatembenuka nati, 'Ndani amene wandikhuza Ine?'

Iye amakhoza kudziwa bwanji mu chipiringu cha wanthu choterocho (mwina gulu lathuli kuchulukitsa makumi katatu - zikwi zikwi zawanthu) anadziwa bwanji nanga? Iye anati, "Ndani wandigwira Ine? Molunjika, Iye anayang'anayang'ana nawona kamzimayiko, pamene anakhala kapena kuyima (kaya anali motani - anamuwuza iye kuti vuto lake la magazi latha. Ameneyo anali Yesu dzulo; ndi yemweyo lero.

Kodi mukukhulupira zimenezo? Ine sindikukudziwani inu; Mulungu akukudziwani. Muli ndi kuwawa kumene kukusautsani. Ndi choncho. Inu muli pamenepo kupemphera Ine ndine mlendo kwa inu? Ndife alendo kwa wina ndi nzake; imani ngati ziri choncho. Ine sindikukudziwani inu. Bambo uyu pakonapa, m'nyamatayu. Inunso mukuvutika pakhosi. Ndi choncho. Mukupemphera za zimenezo; nonsenu muli ndi manjeje ndi chifukwa china chake. Muyenera kuchoka pakati pa msonkhano, chifukwa ndinu mtumiki. Muli ndi zochitika zina zimene muyenera kukakwaniritsa, Ndi choncho. Inu mukukhulupira kuti Mulungu akudziwa kuti inu ndi yani? Rev. Mr. Smith, tsopano pitani kwanu pakhozi panu sipakuvutaninso. Anakhuza ndani?

Bambo amene akhala kumbuyoko akuvutika. Ali ndi chotupa m'mapapo awo kumanzere. Iwo - siwochokera kuno. Mwakhala mukugwira ntchito ya mu m'godi. Ndi choncho. Ine ndi mlendo kwa inu mwathunthu; ngati ndi choncho, gwedezani dzanja lanu. Choputa chiri kumanzere ndipo pakali pano ndinu wokonzekera opareshoni. Ndi choncho? Inu kwanu si kuno, mwachokera kunja kwa mzinda. Mwachokera ku Virginia. Ndi choncho Mukukhulupira kuti Mulungu akudziwa kuti ndinu yani? Mr. Mitchell (Ndi choncho), pitani kumudzi mukakhale bwino. Yesu Khristu wakuchiritsani. Mfunseni bamboyo; sindinamuwone iye m'moyo wanga wonse. Iye amangopemphera pamenepo. Lero Lembo ili...

Pano pali mzimayi amene ali kumbuyo kwangaku, monga Sarah anali mu hema. Iyeyu akupempherera mwana wake wamkazi. Imani Mwanayo sali pano; ali kutali. Mwanayo ali ndi... Inu muli chimodzi modzi ndi mzimayi amene anadza kwa Yesu amene anagwidwa ndi m'dierekezi kowopsya. Mzimayiyo - mwana wake ndi wogwidwa ndi ziwanda. Mwanayo sali pano; iwowa achokera - ndinu a ku North Carolina. Mukukhulupira zimenezo, ndipo zimenezo ndi zowona, si choncho? Mrs. Orders, mukhoza kupita kumudzi kwanu. Ngati mukhulupira ndi mtima wanu wonse, mukamupeza mwana wanu monga momwe Yesu Khristu m'masiku apitawo ananenera.

Lero Lembo ili chizindikiro cha Sodomu, chizindikiro cha Mbewu Yopambana, chizindikiro cha Mpingo wamba - Lero Lembo ili lakwanitsidwa pakati panu! Mukukhulupiri-

ra? Kodi mumulandira Iye nthawi yemweyi monga Mpulumutsi - Mchiritsi wanu? Imirirani aliyense ndi kuti "Ine ndikulandira machiritso anga; ndamulandira Iye ngati Mpulumutsi wanga; ndikumulandira Iye monga Mfumu yanga." Aliyense ayime.

Lero... Tamverani anzanga. Iye anawerenga Malembo, nabwezera Baibulo kwa wansembe, ndipo maso onse anali pa Iye. Ndipo Iye anayang'ana pa iwo nati, "Lero Lembo ili lakwanitsidwa."

Ine ndawerenga Malembo, ndi maumboni ambiri ofotokozera kuti tikukhala m'masiku otsiriza, mbadwo umene udzawona Yesu Khristu akubwerera ku dziko lapansi. Ndipo ndikuti kwa inu usiku unonso, Lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu.

Inu ku Tuscon, inu ku California, inu ku New York, pa matelefoni otcheredwawa, lero Lembo ili lakwanitsidwa pamaso panu! Tiyeni tisangalale ndi kukondwa pakuti Chikwati cha Mwana wa Nkhosa chayandikira, ndipo Mkwatibwi wake - wadzikonzekera!

Tiyeni tikweze manja athu ndi kumupatsa Iye Ulemelero, anthu inu nonse Mulungu akudalitseni.

*This Day This Scripture Is Fulfilled*
*(Lero Lembo Ili Lakwanitsidwa)*

This Message by Brother William Marrion Branham, originally delivered in English on Friday evening, February 19, 1965, at the Parkview Junior High School in Jeffersonville, Indiana, U.S.A., was originally taken from the magnetic tape recording and printed unabridged by Spoken Word Publications. This Chichewa translation was published in 1986 by:

SPOKEN WORD PUBLICATIONS
P.O. Box 888, Jeffersonville, Indiana, U.S.A. 47131

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org